

MAU OYAMBA

Assalam Alaykum, mwaswera bwanji ana anga? Iyi ndi magazini ya Chisilamu yomwe ndakulemberani kuti ndicheze nanu pa nkhani ya Sawm Ramadan. Monga mukudziwa kuti mwezi umenewu wayandikira.

Choyambilira dziwana ana anga okondeka kuti Rasulullah (s.a.w) adati: *“Yemwe angasale mmwezi wa Ramadan mwachikhulupiriro ndi mofuna malipiro kwa Allah, akhululukidwa machimo ake onse omwe adatsogola”*. (Bukhari ndi Muslim).

Dziwaninso ana anga kuti kusala kwa Ramadan ndikokakamizidwa. Ndipo yemwe angasiye kusala kumeneku popanda chifukwa ndiyekuti wachita tchimo, ndipo akalangidwa mmanda komanso tsiku la Qiyamah.

Choncho nzokakamizika kwa aliyense kusiya chakudya ndi chakumwa kuchokera m'bandakucha mpaka kubila kwa dzuwa.

Mmagazini imeneyi ndakubweretserani nkhani ndi mitu yosiyana-siyana. Cholinga chake nchakuti mukhale ana oyikonda Ramadan. Muli nkhani izi;

- Makki kukonzekera Ramadan
- Kodi ana inu mukudziwa?
- Tsiku limodzi isadafike Ramadan
- Miyambo ya Sawm Ramadan
- Kuyanjana mwezi wa Ramadan
- Mapulanu athu Ramadan ikubwerayi

Pomaliza ndikumpempha Allah kuti akudalitseni nonse ndi kulandira Sawm yanu. Khalani ana okonda Ramadan.

Zaid Bunaya, Abu Muhammad

Salima Main Masjid

7 Sha'ban 1441/4 April, 2020

Makki kuikonzekera Ramadan

Tsiku lina Makki adanyamuka kunyumba kwawo kupita kwa nzake Hassaam. Ali mnjira amayankhula yekha-yekha amvekere: “Ndikumpempha Allah kuti ndalama zomwe ndili nazo zikhale zokwanira”.

Kenako anafika kwa nzake Hassaam ndipo anayankhulana motere:

Makki: “Kayfa Haaluk (Uli bwanji) Hassaam?”.

Hassaam: “Al-Hamdulillah, ndili bwino. Nchiyani chakubweretsa kuno?”.

Makki: “Ndabwera kuti ndidzagwirizane ndi Shaykh Ahmad za mphatso ya Ramadan”.

Hassaam: “Mphatso ya Ramadan? Nde chiyani chimenecho?”.

Makki: “Inde, ife tikhala tikupereka mphatso kwa anthu osala mmwezi wa Ramadan ukubwerawu. Tidzipereka tizikwama tokhala ndi timabuku mkati mwake tofotokoza nkhani za Deen yathu ya al-Islam”.

.....komanso ma CD a ma bayan achisilamu”.

Hassaam: “Oh, masha-Allah”.

Atamaliza kukambirana kwawo, Makki ndi Hassaam adanyamuka kupita kwa Shaykh Ahmad. Atafika anakambirana nawo motere:

Shaykh Ahmad: “Kayfa Haaluka Makki, uli bwanji?”.

Makki: “Al-Hamdulillah, ndili bwino”.

Shaykh Ahmad: “Ndi zinthu zanji zomwe ukufuna kuti ndikubweretsere?”.

Makki: “Mmm, ndikufuna timabuku ndi ma CD a mphatso za Ramadan”.

“.....eni, izi ndi ndalama zomwe ndili nazo. Ndingathe kugula mphatso zingati ndi ndalama zimenezi?”.

Shaykh Ahmad: “Ungathe kugula mphatso zokwanira kupereka kwa anthu mwezi omwe wa Ramadan”.

Makki: “Mwati chiani? Allahu Akbar”.

Shaykh Ahmad: “Osadandaula, gawo linalo ndakuwonjezera ndine mokuthandiza. Kodi siukufuna kuti nanenso ndipeze nawo thawab zako?”.

Makki: “Jazakallah, Allah akulipireni zabwino ndipo ndikumpempha kuti alandire mphatso yanu”.

Shaykh Ahmad: “Allahumma Amin. Likangofika tsiku loyambilira mwezi wa Ramadan udzadutsire kuno, udzapeza tizikwama tonse tili tokonzedwa kuti udzatenge”.

Atamaliza kukambirana ndi Shaykh Ahmad, Makki pamodzi ndi Hassaam adanyamuka kubwerera. Ali mnjira adayamba kukambirana motere:

Makki: “Al-Hamdulillah, ichi ndi chinthu chachiwiri mu ma program omwe ndawakonza”.

Hassaam: (modabwa), “wati chiani? Ma program anji amenewo?”.

Makki: “Ndangotsala ndi masiku awiri okha kuti ifike Ramadan. Choncho ndakonzeratu ma program osiyana-siyana kuti ndipindule mokwanira mmwezi umenewu”.

Hassaam: “Nde wakonza ma program anji?”.

Makki: “Ndakonza ma program awa; kupemphera Salaah zonse ku Masjid pamodzi ndi Jamaa`ah, kumaliza kuiwerenga Qur’an yonse ndi kumverera nawo ma Bayan a Deen omwe amachitika mMasjid”.

“.....komanso kupemphera Taraweeh yonse ndi kugawa mphatso za Ramadan”.

Hassaam: “Eya, paja osaiwalanso kugawa chakudya cha Iftaar kwa anthu osala, monga momwe timachitira chaka chilichonse”.

Makki: “Aah!! Ndidaiwala kudutsira kwa Al-Hajj Abdullah kukawauza kuti chaka chinonso ndiwathandiza kugawa chakudya cha Iftaar kwa anthu. Pompano ndikupita kunyumba kwawo chifukwa panopa tili pafupi zedi ndi Shop yawo”.

Nthawi yomweyo Makki ndi Hassaam adayenda mothamanga kupita kwa Al-Hajj Abdullah kukawauza za nkhaniyi. Ndipo attafika kukambirana kwawo kunali motere:

Makki: “Assalamu Alaykum! Kodi Al-Hajj Abdullah alipo?”.

Munthu wachilendo: “Wa Alaykumussalam. Ayi kulibe achokapo. Abwerako pakapita sabata imodzi”.

Makki: “Chiani?”.

Makki anandaula zedi atamva kuti Al-Hajj Abdullah achokapo. Hassaam adamufunsa Makki kuti:

Hassaam: “Nde uchita bwanji pamepa?”.

Makki: “Sindikudziwa, komabe ndili ndi chiyembekezo kuti Allah sangandimane malipiro zimenezi”.

Kenako Makki ndi Hassaam ali mkati mokambirana, adangomva munthu wachilendo uja akuitana

Munthu wachilendo: “Ana inu! Kodi mumamdziwa mwana wina dzina lake Makki?”.

Makki: “Ine ndine Makki”.

Munthu wachilendo: “Al-Hajj Abdullah adasiya envilopu iyi, ndipo adandiwuza kuti ndikupatsire”.

Makki: “Ya ineyo?”.

Makki nthawi yomweyo adatenga envilopu ija ndikuitsegula.

Hassaam: (Kufunsa) “muli chiani mu envilopu imeneyi?”.

Makki: “Sindikudziwa, nditsegule kaye kuti ndidziwe zomwe zili mkati mwake”.

Makki: Al-Hamdulillah, akundifotokozeru mkalatayi kuti mwana wawo Hasan abweretsa katungu wa Iftar lero pa sitima isadachitike Adhan ya Maghrib. Ndipo zonse zikhala mmene timachitira zaka zonse”.

Hassaam: “Al-Hamdulillah, thawab zija zisidawonongeke”.

Makki: “Tsopano ma program onse a Ramadan akwanira”.

Hassaam: “Ineyo ndikuthandizira kukwaniritsa ma program amenewa – insha-Allah, kuti nanenso ndipeze nawo thawab, komanso kuti ndipindule ndi nthawi yanga”.

Choncho Makki adamaliza kukonzekera maprogram ake onse Ramadan isadafike. Kenako patapita tsiku limodzi, Makki akuyenda adamva azibambo awiri akuyankhulana za mwezi wa Ramadan.

Nkhalamba yachikulire: “Madalitso akhale nanu inu bambo ake a Hassaan. Mwezi waoneka”.

Bambo wina: “Allah awubweretse mwezi umenewu kwa ife komanso kwa anthu onse ndi zabwino, mwayi ndi madalitso”.

Makki atamva kukambirana kumeneku adafunso mwachidwi motere:

Makki: “Mwezi waoneka?”.

Azibambo awiri aja: “Inde, Al-Hamdulillah, ndipo mawa ndi tsiku loyamba la Ramadan”.

Makki: Allahu Akbar, Ramadan yabwera! Allahu Akbar, Ramadan yabwera!”.

KODI ANA INU MUKUDZIWA?

- Kuti Salah yoyambirira yomwe adaipemphera Rasulullah (s.a.w) idali Thuhr?
- Kuti munthu oyambilira kukwera pa hatchi adali Ismail (a.s)?
- Kuti Ayah yolemekezeka zedi mu Qur'an ndi Ayatul-Kursi?
- Kuti munthu oyamba kulemba ndi cholemba ndi Idris (a.s)?

TSIKU LIMODZI ISADAFIKE RAMADAN

Marhaban (*ndakulandirani ndi manja awiri*) ndipo khalani omasuka. Ndabwera kuti tikufotokozereni zomwe zidachitika litangotsala tsiku limodzi kuti tilowe mmwezi wa Ramadan.

Lidali siku lodabwitsa zedi.....

Ndipo lidali tsiku losiyana ndi masiku onse....

Ummu anga adagwirizana ndi anzawo oyandikana nawo nyumba kuti adzikumana madzulo aliwonse.

Nkumano wawufupi zedi kunyumba ya mmodzi mwa iwo, kuti adziloweza Qur'an limodzi.

Inde, kanali kankumano kofulumira zedi kosapitilira mphindi 30 zokha.

Lero kwa awa mawa kwa awo.....

Amafuna kuti adzimaliza mofulumira kuti akapitilize ntchito zosiyana-siyana za pakhomu.

Makamakanso podziwa kuti mwezi wa Ramadan wayandikira, ndipo ntchito zimawonjezekera mmwezi umenewu.

Nkumano wawo oyambilira udali mnyumba mwathu. Lidali tsiku limodzi isadafike Ramadan.

Onse adakhala pansu mwa Sunnah ngati azimai achisilamu.....

....nanenso ndidakhala nawo limodzi.....kuti ndiphunzireko kuchokera kwa iwo.

Aliyense atamaliza kuwerenga kwa nzake gawo lake lomwe adaloweza, asadanyamuke kumapita mmakwawo...

Mmodzi wa iwo adati: "Nkumano wathuwu ndi nkumano wa barakah ndi wamadalitso. Aliyense wa inu anabwera pano kufuna zabwino komanso malipiro kwa Allah.

Nde mukuona bwanji titagwirizana kuti tichite ntchito ina yake yabwino tonse limodzi mmwezi ukubwerawu?”.

Onse adayamikira fundoyi ndipo adayamba kupereka maganizo awo.

Kenako Ummu anga adati: “Mukuona bwanji titapanga ntchito yopereka chakudya cha Iftaar ku mabanja osawuka kuti adzifutulira mnyumba zawo?”

“Tiwerenge mabanja osawuka amene tikuwadziwa, ndipo tsiku lililonse tikamaphika chakudya chatu cha Iftaar tidzichichulukitsa”...

“kuti tidziwapatsako mabanja osawukawa mwezi onse wa Ramadan”.

Mmodzi mwa azimayiwa adayankhira mwamphamvu amvekere: “Maganizo abwino zedi, ndipo sindikukaika kuti amuna athu mmanyumbamu agwirizana nawo maganizo amenewa ndipo atithandizira insha-Allah”.

Choncho azimai aja adagwirizana pa fundo imenei....

Ndipo adamwazikana kumabwerera mmakwawo uku ali odzadzidwa ndi chimwemwe.

Onse atatuluka ine ndiwawuza Ummu anga kuti: “Ummi, kodi nzotheka kuti nanenso ndidzakuthandizireni pa ntchito imeneyi?”.

Ummu anga anayankha momwetulira kuti: “Palibe chovuta Habeebah, imeneyi ndi ntchito yabwino. Tonsefe nzotheka kuthandizana komanso kupeza nawo malipiro”.

Miyambo ya Sawm

Pewa kutukwana, bodza, kukangana, miseche ndi machimo onse pamene ukusala.

Munthu wina akakuyamba umuwuze kuti: “***Ine ndikusala, ine ndikusala***”.

Chulukitsa kudzipemphera zabwino kwa Allah pamene ukusala, komanso makolo ako awiri, abale ako ndi anthu onse okhulupirira.

Chulukitsa Thikr ndi kuwerenga Qur’an ndi kukhala mMasjid ndi kumvetsera ulaliki pamene ukusala.

Ukhale otanganidwa kutumikira makolo ako awiri, ndi ma Ulamaa’ ndi asilamu okalamba.

Ukhale wachisoni kwa anthu osawuka ndi ofowoka ndi ana ang’ono-ang’ono pamene ukusala.

Pamene ukuchita Iftaar uyambe ndi kudya tende, ndipo ngati palibe tende uyambe ndi kumwa madzi. Imeneyi ndi Sunnah ya Rasulullah (s.a.w).

Pamene ukuchita Iftaar unene kuti: “***Allaahumma Laka sumtu wa `ala rizqika aftartu***”.

“E Allah! Ndidasala chifukwa cha Inu ndipo ndi chakudya chochokera kwa Inu ndamasula”.

Pomaliza, limbikirani zedi kupemphera Salaah ya Taraawiih ndi Witr pagulu, ndipo usagwere ulesi mwana wanga. Chifukwa kusiya ntchito zimenezi ndiko kuluza ndipo ukadzinena tsiku la Qiyamah.

KUYANJANA MMWEZI WA RAMADAN

Unali mwezi wa Ramadan, Ummu ake a Salma ali ku khitchini bize kukonza chakudya cha Iftaar.

Ummu Salma: “Kodi Salma ukutani?”. Hayya! Tamabwera undithandize kukonza iftaar”.

Salma: (Ali bize kuwerenga magazine ya chisilamu) “Ndikubwera Ummi.....koma sindinamalize kaye kuwerenga magazine ya Ramadan”.

Ummu Salma: “Ungathe kumalizitsa kuwerengako pambuyo pa Iftaar. Hayya! Changu pakuti Asr yatsala pang’ono, tilibe nthawi yambiri”.

Salma: “Chabwino.....koma ndiyambe kaye ndamuimbira foni Habeebah ndi Farhanah”.

Ummu Salma: “Ayi, nthawi yake siino”.

Salma: “Ndingoyankhula nawo mau ochepa chabe Ummi, kuti thawab zanga zisapite padera”.

Ummu Salma: “Thawab zake zitinsu zomwe ukunena iwe?”.

Salma: “Masiku anayi apitawo ndidakangana ndi Habeebah komanso Farhanah”.

Ummu Salma: “Ee?! Mpaka masiku anai?”.

Salma: “Inde, adayesetsa kuti andipepese koma ineyo ndidikanisitsa. Ndimadikira kaye kuti ufike mwezi wa Ramadan nde ndidziyanjana nawo bwino. Paja amati malipiro ndi thawab zimawonjezeredwa mmwezi wa Ramadan. Ndikayanjana nawo panopa ndekuti ndipeza thawab zankhani-nkhani”.

Salma ndi Ummu ake ali mkati moyankhulana, nthawi yomweyo Abu Salma anagododa pa chitseko kulowa mnyumba.....

Abu Salma: “Assalamu Alaykum Warahmatullah Wabarakatuh. Kayfa Haaluki ya Umma Salam?!”.

Ummu Salma: “Wa Alaykumussalam Warahmatullah Wabarakatuh. Tabwerani mundithandize kudabwa ndi kuseka”.

Salma: “Mukudabwa chiani nanga Ummi? Kodi mayesa Allah amawonjezera ntchito zabwino mu Ramadan?”.

Ummu Salma: “Inde, koma zimenzo sikutanthauza kuti mpakana munthu kuchedwetsa kupepesana ndi anzako kudikira ifike Ramadan”.

Abu Salma: “Kodi sukudziwa lwe Salma kuti sizololedwa kwa msilamu kumukwiyira msilamu nzake kupyola masiku atatu?!”.

Ummu Salma: “Komanso Rasulullah (s.a.w) adatiphunzitsa kuti munthu wabwino kwambiri ndi amene amayambilira kumpatsa nzake Salam ndi moni pamene wakangana naye”.

Salma: “Rasulullah (s.a.w) wanena zoon. Pompano ndikuwaimbira ndipo ndiwapepesa chifukwa cha kuchedwetsa kwanga kuyanjana nawo”.

Chomwecho Salma adamuimbira foni Habeebah ndi Farhanah ndikuwapempha kuti amukhululukire pa kuchedwetsa kwake kuyanjana nawo. Ndipo Habeebah ndi Farhanah adavomera kupepesako ndipo adayambanso kuyenderana ndi kumachezera limodzi.....

Mapulani athu Ramadan yomwe ikubwerayi

Ife ndife ana oikonda Ramadan. Insha-Allah ikafika Ramadan tidzipanga izi;

- Tidzipereka madzi ozizira kwa anthu osala
- Tidzisesa ndi kukonza mMasjid kuti mudzikhala mosamalika
- Tidziwathandizira Ummu athu kukonza chakudya cha Iftaar
- Timaliza Juz amma yonse kuwerenga matanthauzo ake
- Tiloweza ma hadeeth 10 a Mtumiki (s.a.w)
- Tidzipemphera nawo Tarawiih ndi Witr ku Masjid
- Tidzipemphera Salah zonse zisanu ku Masjid
- Tidzichulukitsa maduwa mmwezi umenewu

Ife ndife ana oikonda Ramadan. Ife ndife Shabaabu Ramadan!!

ZA MKATIMU

Mutu	Tsamba
Mau oyamba	01
Makki kukonzekera za Ramadan	02
Kodi ana inu mukudziwa?	08
Tsiku limodzi isadafike Ramadan	09
Miyambo ya Sawm	11
Kuyanjana mmwezi wa Ramadan	12
Mapulani athu Ramadan ikubwerayi	14
Za mkatimu	15